# PEMPHO LAKUTI TIMVETSERE NDIPONSO TIKHUDZIDWE NDI MADANDAULO AKULIRA KWA AMALAWI OSAUKA

## *UTHENGA WOCHOKERA KU BUNGWE LA AEPISKOPI AKATOLIKA M'MALAWI – (ECM)*

**10th October 2022**

## Mau Otsogolera

Ife, Aepiskopi Akatolika m'Malawi muno, monga takhala tikuchitira m'mbuyomu pamene dziko lathu likudutsa m'nyengo zovuta, takhala tikupemphera ndi kusinkhasinkha m'mene zinthu ziliri komanso kuyendera pakati pathu. Tachita izi poyang'anira zinene Amalawi tinkayembezera komanso kulakalaka pa nthawi ya chisankho chapitachi. Popemphera mosinkhasinkha, taona ndiponso kumva madandaulo akulira kwa Amalawi osauka pa umphawi wao umene ukunka nukulirakulira m'dziko lino. Tikukhulupirira kuti munthu wina aliyense wounikiridwa ndi choonadi ndiponso wosatsamira pa bodza, akutha kuvomereza zimene tikufotokozazi. Ife, ngati Abusa a mbumba ya Mulungu, sitingalephere kukhala okhudzidwa ndi kulira kwa anthuwa chifukwa, "chimwemwe ndi chiyembekezo chao, madandaulo ndi zokhoma zimene akukumana nazo masiku ano, makamaka anthu osaukitsitsa, zimakhalanso chimwemwe ndi chiyembekezo komanso zokhoma za Akhristu onse" *(Gaudium et Spes, 1).*

Ndi mtima wosweka, tikukumbukira kuti pamene tinkavotera atsogoleri Aboma latsopanoli zaka ziwiri zapitazo, tidali ndi chiyembekezo chonse kuti zimene ankatilonjeza pa nthawi ya kampeni zinali zoona ndi zotitsimikizira kuti tiyamba Malawi watsopano. Mwachisoni ndiponso motayitsa mtima, zikuoneka kuti malonjezo onse aja sakusonyeza zipatso zake monga Amalawi ambiri oganiza bwino akuonera zinthu m'dziko lathuli. Anthu ambiri akuzunzika kuti apeze zosowekera pa moyo watsiku ndi tsiku ndipo umphawi ukunka nuzika mizu pakati pathu. Ngakhale kuti Ngozi

zogwa mwadzidzi ngati madzi osefukira ndi mphepo zamkuntho, komanso mliri wa COVID-19 kuphatikizapo nkhondo yaku Ukraine zatikhudza ndithu, komabe ife tikuganiza kuti, utsogoleri m'dziko lino udalephera kugwiritsa bwino ntchito mwai wosiyanasiyana umene timakhala nawo, kuphatikizapo kulephera kutsata ndondomeko zothandiza ndi kuonetsetsa kuti zinthu zikuyenda bwino. Zotsatira za izi zikusonyeza kuti zinthu m'dziko la Malawi zankirankira kubwerera m'mbuyo poyerekeza zomwe tinkayembekezera pamene maiko ena m'dera lomwe lino amene adaakumananso ndi mavuto omwewo akutukuka mooneka ndithu pa chuma ndinso moyo wao.

Mu uthenga uwu, molumikizana ndi Amalawi ambiri amene ali mu umphawi wadzaoneni, Mpingo Wakatolika, kudzera mwa ife Aepiskopi anu, ukufuna kubwerezanso mau odandaula m'malo mwa anthu osaukawa.

*"Uzilankhulira onse amene sangathe kudzilankhulira; uwalankhulire pa zowayenerera. Uzilankhula ndi kuweruza mwachilungamo. Uziteteza amphawi ndi osauka" (Miyambo 31:8-9).*

Kulira ndi madandaulo a anthu osauka akunka nakulirakulira tsiku lirilonse m'dziko lathu lino. Zina zimene zikuchititsa anthu kuti azidandaula ndi monga kuchepa kwa mphamvu ya ndalama yathu, kukwera kwa mitengo ya chakudya, kusowa kwa ntchito pakati pa achinyamata, kukwera kwa fizi zolipirira sukulu, kuperewera kwa chithandizo cha umoyo, kusowa kwa mafuta komwe kwachititsa kuti mayendedwe akhale odula, mchitidwe wa anthu ena a mabizinezi wokweza mitengo ya malonda ao mosaganizira anthu osauka, kusowa kwa ndalama zakunja ndinso kuperewera kwa ndondomeko zotetezera anthu ogula. Kuti mayankho ku zodandaula ndi kulira kwa anthu osauka apezeke, pasoweka kukhazikitsa ndondomeko ndi Mfundo zabwino komanso zotheka. Ndondomeko zabwino zimene zilipo kale, zikulephereka kugwira ntchito pa zifukwa monga katangale, ndondomeko zoipa zoyendetsera zinthu m'dziko, njira zosakhazikika zothandiza ndi kuonetsetsa kuti ogwira ntchito m'boma akugwiradi ntchito yao mokhulupirika, chithunzi chosaoneka bwino cha m'mene ulimi uyendere chaka chino ndiponso njira zobwerera m'mbuyo za m'mene Boma la Tonse Alliance likuyendetsera dziko.

## 1. Kuipa kwa Katangale

Takhala tikulankhulapo m'mbuyomu za kuipa kwa katangale ndi mmene pang'onopang'ono akuzikira mizu pakati pathu. Khansa wa katangale wasanduka ngati mchitidwe wochitira zinthu ndi wovomerezeka m'Malawi muno. Katangaleyu akusokoneza ndi kuwononga zinthu munthambi zosiyanasiyana zoyenera kutumikira nzika za dziko lino. Malonjezo amene Aboma la Tonse Alliance ankalonjeza pa nthawi ya kampeni adaachititsa Amalawi kuti akhale ndi chiyembekezo chakuti katangale atheratu. Koma mmene nkhondo yolimbana ndi katangale ikuyendera, ikutichititsa kuti tikhale ndi mafunso ochuluka kuposa mayankho. Tikudzifunsa kuti: *Kodi pali kulumikizana ndi mgwirizano wokhazikika pakati pa madipatimenti Aboma omwe adapatsidwa udindo pa nkhani yolimbana ndi katangale? Nchifukwa chiani nkhani za katangale zokhudza andale ndi anthu ena abizinezi zikuoneka ngati zidangoyima? Nchifukwa chiani nkhani zina zomwe zidaperekedwa ku Bungwe Lothetsa Ziphuphu zimachedwa kufufuzidwa? Kodi pali ena amene akutetezedwa? Kodi zimene zimakambidwa pagulu kuti tithetse katangale zimalankhulidwa moonadi kapena ndi zongofuna kuteteza zofuna za anthu ena ochepa andale?*

Ife tikukhulupirira kuti utsogoleri wabwino ndi wochita zinthu molimba mtima, makamaka pa nkhani zazikuluzikulu za katangale zokhudza anthu otchuka ndi apamwamba, utha kutsimikizira anthu kuzindikira kuti Boma latsimikiza kuthetsa mchitidwe woipawu m'dziko lathu lino. Koma ngati utsogoleri wotere palibe, anthu amataya chiyembekezo. Mpingo ukuganizanso kuti ndondomeko zina zimene zimatsatidwa powunikira malamulo ozengera milandu yakatangale, zimachititsa kuti nkhondo yolimbana ndi katangale isamayende bwino. Amalawi amayembekeza kuti Bungwe Lothetsa Ziphuphu (ACB), Dipatimenti ya Boma Younikira milandu yoyenera kuzengedwa (DPP), Ofesi Yolangiza Boma pa nkhani za malamulo (Attorney General), Ochita kafukufuku pa nkhani ya zachuma ndi Apolisi ofufuza milandu ya zachuma (Fiscal Police) ayenera kumagwirira ntchito zao modalirana ndi molumikizana poyang'anira ubwino wadziko lathu. Ife, Aepiskopi Akatolika, ndife okhumudwa kuona kuti anthu ena amene m'mbuyomu ankateteza ndi kulankhulira anthu osauka ndi amphawi m'dziko lathu lino, tsopano amalankhulira ndi kuteteza anthu olemera. Ndizomvetsa chisoni kuti iwowa adasiya anthu osauka kwambiri amene akuyenda mu mdima wa umphawi pamene akufunafuna chilungamo pa nkhani ya za chuma komanso umoyo wao. Ngakhale tikudziwa kuti nkhani zakatangale ndizovuta makamaka pamene mchitidwewu wazika mizu kuphatikizapo m'ndondomeko ya kagwiridwe ka ntchito, komabe tikupempha onse amene adapatsidwa udindo wothetsa mchitidwewu kuti agwire ntchito yao mokhulupirika m'malo mwa nzika za m'Malawi muno.

## 2. Kulephera kupereka zosowekera pamoyo wa anthu: *Zizindikiro zakulephera kwa Boma*

Ndizomvetsa chisoni kuti nzika za dziko lino zikulephera kupeza chithandizo ndi zosowekera pa moyo wao zomwe, kuonjezera pa katangale, zimachitika pa zifukwa monga kuchepa kwa ndalama zimene madipatimenti osiyanasiyana amalandira, kusowa kwa zinthu zina zofunikira, mkhalidwe woipa wa ogwira ntchito ena m'boma amene safuna kudzipereka pantchito, kusowa kwa zinthu zina monga mafuta agalimoto ndi kuzimazima kwa magetsi. Izi zakhudza zintchito ya zaumoyo, maphunziro, ulimi, kupezeka kwa madzi abwino aukhondo, mayendedwe, ndi zina zotero. Izi ndi zizindikiro zakuti zinthu sizikuyenda bwino m'mdziko lino ndipo tivomere kuti Boma lalephera. Ndizomvetsa chisoni ndipo sichilungamo kuti anthu ambirimbiri azivukitika ndi umphawi wadzaoneni pamene anthu ophunzira oyendetsa boma akusangalala ndi kukhala moyo wapamwamba pogwiritsa ntchito ndalama za msonkho wopereka anthu osauka. Ife, Aepiskopi Akatolika tikufunsanso kuti: *Kodi Amalawi ngosayenera kukhala ndi moyo wabwinopo kuposera ali nawo masiku ano?*

## 3. Kulephera kotsata mfundo zokonzera zinthu m'dziko

Boma limene limamvetsera ndi kudziwa zimene zikusautsa anthu m'dziko limachita zinthu mosonyeza kuti likukhudzidwa ndi mavuto amoyo komanso achuma amene nzika zikukumana nawo. Pachifukwa ichi, ife tidaayamikira ndi kukondwera pakumva kuti Boma lakhazikitsa njira zothandiza kuti chuma cha dziko chisamagwiritsidwe ntchito mwachisawawa ngati njira yobwezeretsa m'chimake mavuto achuma amene akhudza dziko lino. Koma poona zimene zikuchitika, Amalawi ambiri akudzifunsa mafunso ambiri opweteka osonyeza kuti zija Atsogoleri athu aboma ankanenazi, zinali nkhambakamwa chabe. Mafunso ena amene anthu akudzifunsa ndi monga awa: *Kodi zimene akuchita atsogoleri athu andale ndi akuluakulu ena m'Boma,*

*sizikutsutsana ndi zimene adaalonjeza kuti akhwimitsa njira zochepetsera kumwaza chuma cha dziko mwachisawawa? Kodi zimene tikuonazi sichizindikiro chooneka poyera cha uchiphamaso? Kodi utsogoleri wa dziko lino sindiye unayenera kukhala chitsanzo chosasakaza mwachisawawa chuma cha dziko lino? Nchifukwa chiani atsogoleri adziko lino akudzitsutsa okha pa zimene adaanena okha pomachita maulendo ena opita kunja kwa dziko lino – maulendo ena opita ndi chigulu chachikulu cha anthu – maulendo omwe Amalawi ambiri akuona ngati ndiongosakaza chuma cha dziko? Kodi maulendo oterewa, sakutsutsana ndi zomwe adaatiwuza kuti achepetsa kugwiritsa ntchito chuma cha dziko lino mwachisawawa? Kodi ndondomeko zochepetsera kumwaza chuma cha dziko zidalengezedwa zija, zidalizongotibwatika nazo chabe?* Tikupempha Boma kuti liganizire bwino mafunso amenewa ndipo adziwe kuti ufulu wa Amalawi uyenera kulemekezedwa powayankha momveka bwino pankhawa zawozi.

## 4. Nkhawa za anthu pa ulimi wa nyengo yamvula ikubwerayi

Monga takhala tikunena motsindika m'mbuyomu, chakudya ndi chinthu chofunikira kwa anthu onse. Kuti m'dziko lathu la Malawi mukhale chakudya chokwanira, anthu amadalira ndondomeko yopezera zipangizo zaulimi zoperekedwa ndi Boma (Affordable Inputs Program (AIP). M'zaka zambuyomu, Mpingo udaona kuti ndondomeko yopezera zipangizo zaulimiyi yakhala ikukumana ndi mavuto osiyanasiyana ngati kusiyidwa kwa alimi ena oyenera kulandira thandizoli. Ena mwa mavuto amene akudetsa anthu nkhawa pa nkhani imeneyi moganizira dzinja likubwerali ndi monga kusowa kwa mapulani abwino ofunikira pa ntchito yogawa zipangizozi, kusowa kulumikizana kwenikweni pa ntchitoyi, kulephera kowunikiranso bwino m'mene ntchito yogawa zipangizo za ulimiyi ikuyendera komanso mauthenga omveka bwino chifukwa sizikudziwika kuti kaya chaka chino ndondomekoyi iyenda bwanji. Poona kuti dzinja layandikira kale, anthu ayamba kale kutaya mtima kuti ndondomekoyi siiyenda bwino chaka chino. Zikuonekeratu kuti kutha kudzakhala njala yaikulu chaka chikubwerachi. Tikupempha Boma kuti lichite machawi pankhaniyi ndikuonetsetsa kuti pasakhale munthu wosowa chakudya pakati pathu.

## 5. Kufunika kounikanso ndondomeko zoyendetsera Boma la Tonse Alliance

Amalawi adaponya voti ndi kuthandiza kuti m'dziko lino mukhale Boma latsopano. Amalawi azindikira mokhumudwa kuti kayendetsedwe ka Boma la Tonse Alliance kachuluka miseche, mikangano ndi mpikisano wapansipansi pofuna kutchuka, kukonderana anthu apachibale, kuchita zinthu modzikonda ndi kusagwirizana kwa magulu osiyanasiyana a m'Bomali potsata ndondomeko ndi Mfundo zosiyanasiyana zoyendetsera Boma. Izi ndi zodetsa nkhawa chifukwa palibe m'gwirizano pakati pa magulu osiyanasiyana amene adapanga Boma la Tonse Alliance. Dziko silingatukuke pamene palibe mgwirizano wofunikira ndipo amene akuvutika chifukwa cha zimenezi ndi anthu osauka ndi amphawi. Amalawi atopa tsopano ndi atsogoleri andale amene amalimbirana maudindo kuyambira pamene nyengo yovota isanafike, nthawi yachisankho ngakhalenso pambuyo pa chisankho mosaganizira zosowa ndi chitukuko cha nzika zimene zidawavotera kuti alowe m'Boma. Tikupempha Boma la Tonse Alliance kuti, monga atsogoleri a dziko lino, agwire ntchito mogwirizana kuti zinthu zisinthe m'Malawi muno.

## 6. Kupereka maganizo ndi kupempha kuti adindo achitepo kanthu

Kuchokera pamene tidayamba Malawi watsopano, Mpingo Wakatolika wakhala ukuthandiza kuti m'dziko lathu lino mukhale chitukuko chenicheni kudzera m'nkhani ya maphunziro, ntchito ya zaumoyo, mapologram ena otukula miyoyo ya anthu, kuphunzitsa zokhudza dziko (civic education) ndi ntchito zina zothandiza kudzetsa mtendere ndi umodzi pakati pathu. Ife, Aepiskopi Akatolika timakhulupirira kuti ntchito tikuchitazi ndi gawo limodzi lofunikira la utumiki wathu umene Mulungu adatipatsa. Ndi udindo wathu kulankhulira anthu kuti dziko lathu lizitsata njira zolondola pochita zinthu ndi kuti chitukuko chenicheni chifikire Amalawi onse. Pofuna kulimbikitsa chiyembekezo cha anthu kuti dziko la Malawi litha kukhala lokoma kwa aliyense ndipo pofuna kuti zinthu zimene Chauta adatipatsa mwaufulu wake zikhalire ndi kuthandiza aliyense m'zosowa zake zonse, ife Aepiskopi Akatolika tikupereka malangizo ndi maganizo otsatirawa kuti Boma lichitepo kanthu:

a. Adindo amene adapatsidwa ntchito yolimbana ndi katangale aonetsetse kuti pali kulumikizana ndi mgwirizano pankhondo yolimbana ndi matenda owopsawa pakati pathu;
b. A President ndi Boma lao atulutse poyera repoti limene gulu lomwe lidafufuza ndi kupereka maganizo pa ndondomeko zothandiza kukonzanso kagwiridwe ka ntchito m'dziko lino – (Public Sector Review Systems Taskforce's report);
c. Utsogoleri wa dziko lino ukhazikitse ndi kuonetsetsa kuti ndondomeko ndi mlingo wofunikira wothandiza magulu ndi mabungwe am'boma otumikira anthu, zonsezi, zili m'malo mwake - (Public Sector Reform Programme);
d. Ofesi ya a President ndi nduna zao aonetse ndi zitsanzo zabwino zakuti iwowo sakufuna kumwaza chuma cha dziko lino mwachisawawa pofuna kukwaniritsa njira zokonzanso zinthu m'dziko lino;
e. Pakhazikitsidwe ndondomeko zotetezera anthu pa mavuto amene amphawi akukumana nawo m'moyo wao ndiponso pakhale chitetezo chokwanira cha amene amagula zinthu kuti asaponderezedwe ndi anthu a mabizinezi omwe amakweza mitengo ya zinthu mosaganizira anthu osauka;
f. Boma lipeze njira zokonzera ndi kuchepetsa kusowa kwa zinthu zofunikira ndiponso chuma pamoyo wa alimi ndi amabizenezi ang'onoang'ono;
g. Boma, kudzera mu Unduna wa Malimidwe, liwonetsetse kuti ndondomeko yogawa zipangizo zaulimi m'chaka cha 2022/2023 yakonzedwa bwino ndipo kuti idzachitika mwachilungamo;
h. Boma lichitepo kanthu pa nkhawa zimene Amalawi ali nazo zakuti m'dziko lino mutha kukhala njala yaikulu;
i. Magulu onse a Boma la Alliance aleke kuchita ndale zamiseche pomachita zinthu ngati kuti kampeni ya zisankho ya 2025 yayamba kale. M'malo mwake, ayendetse Boma la Malawi mwachilungamo ndi kuika mtima pachitukuko chenicheni cha dziko lino;
j. Amalawi aonetsetse kuti akukwaniritsa udindo ndi ufulu wao wotenga nao mbali m'zochitika m'dziko lathu monga powonetsetsa kuti adindo onse akugwiradi mwapoyera ntchito imene tidawavotera.

**Pemphero lopempherera dziko lathu**

*Inu Mulungu, ndinu Mulungu wachilungamo. Mumasamala iwo amene amaponderezedwa. Mukakonda iwo amene saganirizidwa. Tikupempha chilungamo ndi chipulumutso m'dziko lathu lino. Muthandize Fuko lathu kuti lizindikire zomwe zikulakwika komanso zomwe tikuchita bwino. Mupatse mtendere ndi chiyembekezo kwa onse amene akuvutika chifukwa chosowa chilungamo pakati pathu – makamaka amene akuvutika pankhani ya chuma kuphatikizapo zoipa zina zomwe zimachotsa ndi kupeputsa ulemerero umene munthu amayenera kuwukondwerera ndi kukhala nawo. Azindikiritseni kuti Inu muli nawo ndipo mumawasamala, ndinso kuti tsiku lina mudzakonzanso zinthu zonse kuti zikhale bwino. Dzazani Fuko lathu ndi chikondi, chifundo komanso chilungamo pa moyo wathu watsiku ndi tsiku komanso pa nkhani ya chuma. Amen. (cf. Miyambo 21: 15).*

| | |
|---|---|
| **Most Reverend George Desmond Tambala,** | **Wapampando wabungwe la Maepiskopi kuno ku Malawi, Arkiepiskopi wa Arkidayosizi ya Lilongwe,** |
| **Right Reverend Montfort Stima,** | **Wachiwiri kwa wapa Mpando wabungwe la maekiskopi kuno ku Malawi ndinso Episkopi wa Dayosizi ya Mangochi** |
| **Most Reverend Thomas Luke Msusa,** | **Arkiepiskopi wa Arkidayosizi ya Blantyre** |
| **Right Reverend Peter Musikuwa,** | **Episkopi wa Dayosizi ya Chikwawa** |
| **Right Reverend Martin Mtumbuka,** | **Episkopi wa Dayosizi ya Karonga** |
| **Right Reverend John Ryan,** | **Episkopi wa Dayosizi ya Mzuzu** |
| **Right Reverend Peter Chifukwa,** | **Episkopi wa Dayosizi ya Dedza** |